

MAPEMPHERO A UMRAH

التشييو CHICHEWA

Kuzungulira
Kaaba(Twawaf)

2

POYAMBILA POTHERA.

Kuzungulira ma
round asanu ndi
awiri (7), kuyambila
pamene pali mwala
WAKUDA
kukatheranso
pamene pali
mwala
WAKUDA
pomwepo.

Malo opangira Niya kapena kuvalira
ihram kwa anthu ochokera ku Shami
ndi Egypt ndi otchedwa: al-Juhfah
mtunda otalika 186 kilometers kuti
akafike ku Makkah .

Anthu ochokera ku Madinah
malo awo ndi otchedwa:
al-Dhul-Hulayfah, mtunda
otalika 420 kilometers.

Anthu ochokera ku Iraqi malo
awo ndi otchedwa: Dhatu-Iraq,
pa mtundu
otalika 98 kilometers.

Anthu ochokera ku dera la Najid,
malo awo ndi otchedwa:
Qarin al-Manāzil,
mtunda otalika 99 kilometers.

Ndipo anthu ochokera ku Yemen,
malo awo ndi otchedwa:
Yalamulam.

1

Kuvala nsalu
ya ihram

Kupanga Niyah
yolowera mu
mapemphero
a Umrah

Anthu amene akubwera pa
ndege, malo awo opangira
ihram adzakha omwe ali
pafupi ndi iwowo, potengera
point iliyonse imene iwo
angaoloke m'mambamo,
m'malo onse tatchula aja.

Ma round asanu ndi awiri (7)

Kenako kukathamanga pakati pa Phiri la
al-Aswafā ndi al-Mariwā, utha kumayenda
usanafike pa zizindikiro ziwi za green, ndipo
umayenera kuthamanga ukafika pamene pali
chizindikiro choyamba cha green cho kukathera
pamenenso pali chizindikiro cha green china.
Uzithamangako kwambiri, ndipo zimenezi
zinaikidwa kwa amuna kuti azithamanga malo
amenewa, akazi ayi.

al-Mariwā

al-Aswafā

kukathamanga pakati pa Phiri
la al-Aswafā ndi al-Mariwā,

4

KUSWALIRA PAMBUYO PA MALO
AMENE AMAIMA IBRAHIM,
NGATI ZITATHEKA KUTERO.

3

Zoletsedwa kwa
yemwe walowa
mmapempherowa:

1 Kuchotsa tsitsi la mmutu kapena pathupi mu njira iliyonseyo.

2 Kuwenga zikhadabu.

3 Kugwiritsa ntchito mafuta onunkhira.

4 Kumangisa nikkah yako kapena yawina.

5 Kukhala malo amodzi ndi mkazi wako.

6 Kupha zinyama za pamtunda
(kupanga ulenje).

1 Kuvala chovala chosokedwa, ndi ndi chovala chomwe
chasokedwe mosiyaniitsa ziwalo za thupi, munga panti, talauza
kapena malaya, ndiye mukutulukamo chosokedwa ngati siketi.

2 Kuphimba kumutu ndi chilichonse chomwe chingagundane
ndi mutu, munga chipewa, nduwila. Ambulera siikulowa nawo.

1 Kuphimba nkhope ndi parada(niqab) kapena burukha,
koma ngati pamalopo pali amuna achilendo ndiye
atha kuphimba nkhope yake ndi chilichonse.

2 Kuvala ma gulovesi.

Kumeta mpala
kapena kuyepula

5

Mpala kapena kuyepula
mutu onse, izi ndi za
amuna, pamene akazi
adzayepula tsitsi lawo
ataliphatikiza, pa mulingo
wa nsonga ya chala.

Mtundu wa zinthu zoletsedwa kwa
amuna okha:

Mtundu wa zinthu zoletsedwa kwa
akazi okha:

Zomwe zili zabwino (Sunnah)
kwa munthu yemwe akupanga Umrah:

- 1 Kuwenga zikhadabu, ndi kuchotsa tsitsi limene limafunika kuchotsedwa munthu asanapange niyah ya ihram.
- 2 Kusamba usanavale ihram.
- 3 kuzinunkhiritsa pathupi usanavale ihram. izi kwa amuna okha akazi ayi.
- 4 Kuvala nsalu ziwi ya mmusi ndiya muntunda, zonse zoyera, amuna okha okha.
- 5 Kunena Talibia: (Labbaika Allahumma Labbaika. Labbaika lā sharieka laka Labbaika. Innal-hamda, wannaamata laka wal-mulik. Laa sharieka laka). Kuyambila pamene tapangira ihram kufikira popangira Twawaf.
- 6 Kuvundukula phewa lakumanja, izi zimatchedwa kuti: idh-twiwāu. Zimenezi apange amuna okha.
- 7 Kuukisa (kupsompsona) mwala wakuda.
- 8 Kuyenda monjonjola(mosathamanga kwambiri monyamula mapazi) izi kupanga ma round atatu oyambilira pozungulira Kaaba.
- 9 Kuswali ma rakah awiri pambuyo pa maqaam Ibrahim, pamene amaima pomanga Kaaba.